STANDARD 4 B/K by emmanuel kapachika

PANGANO

Pangano ndi mgwirizano wapakati pa anthu awiri kapena angapo.

PANGANO LA MULUNGU NDI ABRAHAMU

Mulungu adapanga pangano ndi Abrahamu namulonjeza kuti adzampatsa dziko iye ndi mbewu za pambuyo pake.Mulungu adachita pangano ndi Abrahamu kuti kudzera mwa iye,mitundu yonse idalitsike

NDANDANDA WA BANJA

Ndandanda wabanja umasonyeza ubale wa anthu kuyambira makolo oyambirira kufikira zidzukulu.

ABRAHAMU MONGA TATE WA MITUNDU

Pamene Abramu adali ndi zaka makumi asanu ndi anayi, Mulungu adamuonekera.Adamulonjeza kuti adzakhala tate wa khamu la mitundu,chifukwa cha ichi,dzina lake lidasintha kukhala Abrahamu.

Sarah mkazi wake,adabala mwana namutcha Isaki monga mwa lonjezo la Mulungu

ISRAELI NDI OWERUZA

TANTHAUZO LA MAWU OTI OWERUZA

Oweruza ndi munthu amene amapereka chigamulo cha chilungamo pankhani yakusamvana pakati pa anthu awiri ,magulu aanthu kapenanso mayiko.

UDINDO WA OWERUZA MASIKU ANO

.Kuona za malamulo

.kuthetsa zokangana

.kukhazikitsa bata

.kuteteza ufulu wachibadwidwe wa anthu

OWERUZA AKULUAKULU A ISRAELI

.Deborah

.Gideon

.Yefita

.Samson

Mulungu amasankha oweruza kuti akawalanditse a Israeli

1.DEBORAH

Mulungu adasankha Deborah m'neneri wa mkazi,mkazi wa Lapidoti kuti akupulumutse a Israeli m'manja mwa a Kanani. Deborah ndi Baraki,mkulu wankhondo adangonjetsa a Kanani

2.GIDEON

Mulungu adasankha Gideon kukapulumutsa a Israeli kwa aMidyani.Gideon adagonjetsa a Midyani miyandamiyanda ndi amuna 300 okha chifukwa Mulungu adali naye.

3.YEFITA

Mulungu adasankha Yefita kukapulumutsa a Israeli m'dzanja la Amoni. Yefita adangonjetsa Amoni chifukwa Mulungu adali naye.

4.SAMSON

Mulungu adasankha Samson kukapulumutsa a Israeli m'dzanja la AFilisiti. Panthawi imene adali moyo ndi pa imfa yake,Samson adapha A Filisiti ambiri

TANTHAUZO LAMAWU OTI CHIKONDI

Chikondi chimatanthauza kukhala ndi khumbo loonetsera kapena kuchitira anthu ena zabwino.

MMENE ANTHU AMAONETSERA CHIKONDI

.Kuthandizana ntchito ya m'kalasi

.kulondolera anthu osaona njira

.kulima mmunda mwa anthu okalamba

.kuteteza anthu omwe ali m'mavuto osiyanasiyana

MMENE YESU ADAONETSERA CHIKONDI

.Pochilitsa akhungu

.podyetsa anthu ambiri ndi mikate isanu ndi nsomba ziwiri

MUTU 4. UFULU NDI UDINDO

Ufulu umatanthauza malamulo okhazikitsidwa mwachilungamo cha momwe anthu angamakhalire.

ZITSANZO ZA UFULU

- Kukhala ndi moyo
- Kutetezedwa
- Kusungiridwa chinsinsi
- Kuweruzidwa mwa chilungamo
- Kuphunzira

UDINDO

Udindo ndi ntchito yomwe munthu ayenera kuchita kapena kuchitira wina monga mwa chikhalidwe.

ZITSANZO ZA UDINDO

- Makolo kusamalira ana
- Makolo kuteteza ufulu wa ana
- Wosaononga ufulu wa ena
- Kulemekeza ena
- Kukwaniritsa ntchito yomwe ayenera kuchita

KUFOTOKOZA ZOMWE BAIBULO LIKUNENA ZA UFULU NDI UDINDO

Baibulo limaphunzitsa za ufulu wa anthu ndi udindo wawo. Mwachitsanzo,pamene Kaini adapha mbale wake Abele,Mulungu sadafune kubwezera chilango chakupha.

M'nkhani ya mwana wolowerera,udali udindo wake wosankha zabwino kapena zoipa. Ndipo mu nkhani ya Yosefe ndi abale ake atamupangira chiwembu choti amuphe,Rubeni adawaletsa anzake ndi cholinga choti amupulumutse. Nkhanizi zikuonetsa kuti aliyense ali ndi ufulu.

MUTU 5 ESAU NDI YAKOBO

Zomwe ana ayenera kuchita

Chisamba ndi mwana woyamba kubadwa m'banja.

Mwana wachisamba amabweretsa chisangalalo m'banja. M'myambo yambiri,mwanayi akakhala wamwamuna ndi amene amatenga chuma cha bambo ake akamwalira.

ZA ULOSI WA ANA AMAPASA A ISAKI

Ulosi ndikunena zomwe zidzachitike m'tsogolo.

Mulungu adalosera za kubadwa kwa mapasa a Isaki.

Anawa amalimbana m'mimba mwa mayi wawo kusonyeza mitundu iwiri yomwe idzakhala youkirana.

Izi zimatanthauza kuti mtundu wina udzakhala wamphamvu kuposa unzake. Mwana wamkulu adzatumikira wamn'gono. Monga mwa mwambo wachiyuda,mwana woyamba wamwamuna ndi amene ayenera kulandira madalitso atate ake asanamwalire.

MOMWE ESAU NDI YAKOBO ADAGANIZIRA PA ZA UDINDO WA MWANA WOYAMBA

Esau adali mlenje pamene Yakobo adali kuthandiza amayi ake ntchito zapakhomo. Pamene Esau ankachokera kosaka adali ndi njala ndipo adagulitsa ukulu wake mosinthana ndi mphodza za m'ngono wake.

Isaki atakalamba adatuma Esau kukamuphera nyama m'tchire kuti adzamukonzere chakudya chokoma kuti adzamudalitse. Rabeka atamva izi adamuuza Yakobo kukakonza kamwana ka mbuzi ndi kukonza chakudya chokoma kuti bambo ake adzamudalitse m'malo mwa mkulu wake. Izi zikusonyeza kuti Yakobo adali ndi chidwi ndi nkhani ya ukulu kusiyana ndi mkulu wake. Izi zikuonetsanso kuti Rabeka adathandiza kukwaniritsa ulosi wa amene adzalandire madalitso.

ZA MALOTO

Maloto ndi maganizo ndi zideruderu zomwe munthu amaona ali mtulo. Maloto ena amakhala ovuta kutanthauzira pamene ena osavuta

Ayuda amakhulupirira maloto. Mwachitsanzo,m'maloto a Yosefe,atate ake adakhulupirira kuti iye adzakhala mtsogoleri wawo.

MALOTO A YAKOBO

Yakobo ali pa ulendo wopita kwa malume ake Labani ku Harani,adagona pa Beteli atatsamira mwala. Iye adalota makwelero ochokera pansi mpaka kumwamba pomwe Mulungu

adamulonjeza kuti adzachulukitsa mtundu wake,adzamuteteza ndi kumubwezeretsa kudziko la kwawo.

M,maloto ena , Mulungu adamuuza iye kuti wachulukitsa mbuzi zake zomwe ndi zamipyololomipyololo (mizeremizere),zamathothomathotho ndi maangamaanga. Mulungu adakwaniritsa malonjezano ake mpaka pamene Yakobo adabwerera kudziko lakwawo

KUKHALA MWAMTENDERE

Kukhala mwamtendere ndi kukhala mwabata ndi mosasokonezedwa. Anthu okhala mwamtendere amagawana zosowa zawo ndipo akayambana amakambirana mwamtendere ndi kukhululukirana

NKHANI ZA M'BAIBULO ZA KUKHALA MWAMTENDERE

Yesu adaphunzitsa za kukondana wina ndi mnzake ndi kukhala mwamtendere. Mwachitsanzo, Yesu adadzudzula wophunzira wake yemwe adadula khutu la kapolo wa mkulu wa wansembe,nalibwezeretsa m'chimake. Akhristu amaphunzira za kukondana wina ndi mnzake ndi kusabwezerana choipa

MUTU. 7 HIV NDI EDZI

MMENE TINGASAMALIRE ODWALA

- Kuwapatsa chakudya chokwanira ndi chopatsa thanzi
- Kupita nawo kuchipatala
- Kuwachereza

MMENE AKHRISTU AMASAMALIRA ODWALA

Pamene Yesu ali padziko lapansi adaonetsa chikondi ndi chifundo kwa odwala. Iye adachiza nthenda zosiyanasiyana,nalamula ophunzira kuti atsatire chitsanzochi. Baibulo limaphunzitsa kuti Akhristu ayenera kusamalira odwala ndi kuwapempherera.

MMENE AKHRISTU AMASAMALIRA ODWALA HIV NDI EDZI

Amene ali ndi HIV ndi Edzi angathe kudwalanso matenda monga

- Chifuwa chachikulu
- Kutsekula mmimba

- Matenda a pakhungu
- Khansa
- Chibayo

Osamalira odwala ayenera kukhala opirira,achikondi ndi achifundo

Akhristu sayenera kusala odwala HIV ndi Edzi. Odwala HIV ndi Edzi ayenera kulimbikitsidwa mmoyo wawo wauzimu kuti akhale ndi moyo nthawi yaitali.

MUTU 8 TANTHAUZO LA KUKALAMBA

Kukalamba kumatanthauza munthu amene ali ndi zaka zambiri zukubadwa

MMENE TINGASAMALIRE OKALAMBA

- Kuwatungira madzi
- Kuwaphikira
- Kuwachapira
- Kuwasamalira pakhomo
- Kuwathandiza akadwala

MMENE AKHRISTU AMASAMALIRA OKALAMBA

Baibulo limaphunzitsa kufunika kosamalira,kuteteza ndikulemekeza okalamba. Mwachitsanzo,Yosefe adasamalira atate ake atakalamba mpaka kumwalira. Koma padali ana ena aku Gilgali amene adanyoza Elisa chifikwa cha dazi ndipo adawatemberera nadyedwa ndi chimbalangondo(chilombo cham'tchire)

MUTU 9 CHIPHUNZITSO CHA YESU PA ZACHIKONDI

Chikondi chimatanthauza kuchitirana zinthu zabwino pabanja.

MMENE MAKOLO AMASONYEZERA CHIKONDI PA ANA AWO

- Kuyamwitsa makanda mokondwera
- Powapatsa mphatso

MMENE ANA AMAONETSERA CHIKONDI KWA MAKOLO

- Pomvera ndi kugwira ntchito za pakhomo

ZA CHIKONDI CHA YESU PA ANA

Anthu ena adadza nato tiana kwa Yesu kuti atidalitse ndi kutipempherera koma ophunzira ake adawaletsa. Yesu adawauza kuti alole tiwana tidze kwa iye pakuti ufumu wakumwamba uli watotereti. Apa Yesu adawonetsa chikondi chake chopambana kwa ana

KUFOTOKOZA ZA CHIKONDI CHA YESU KWA OCHIMWA NDI ADANI

Afalisi ndi akuluakulu achipembezo ena amadana ndi amisonkho chifukwa cha ntchito yawo ndipo adali kuwaganizira kuti adali ochimwa. Ngakhale zidali choncho,Yesu ankacheza ndi kudya nawo pamodzi,zomwe zidali zotsutsana ndi chipembedzo chawocho. Zonsezo zikusonyeza kuti Yesu adadza chifukwa cha anthu ochimwa osati olungama.

ZACHIKONDI CHA YESU KWA AYUDA NDI AMITUNDU

Yesu adakana kuchiritsa buthu la mayi yemwe adali wa amitundu. Chifukwa cha chikhulupiriro chake mwa Yesu,buthulo lidachilitsidwa.

Munkhani ya Yesu ndi mkazi yemwe adakumana naye pachitsime,mkaziyo adakana kumupatsa Yesu madzi akumwa chifikwa adali m'Yuda. Atakambirana ndi mkaziyo pachitsime , umboni wa mkaziyo ndi chiphunzitso cha Yesu, anthu onse adakhulupirira. Nkhanizi zikuonetsa chikondi cha Yesu kwa aYuda ndi amitundu.

MUTU 10 KUFA NDI KUUKA KA AMBUYE YESU

<u>Kufotokoza za kufa ndi kuuka</u>

Imfa ndi mapeto a moyo. Pamene kuuka ndikukhalanso ndi moyo.

ZA IMFA YA AMBUYE YESU

Yesu ndi ophunzira ake adapita ku phiri la Azitona kukapemphera

. Ali kumeneko, Yudasi mmodzi mwa ophunzira ake adam'pereka kwa adani ake.

MAZUNZO OMWE YESU ADAKUMANA NAWO

- Adanyozedwa
- Adakwapulidwa

Poyamba yesu adampititsa kwa akuluakulu achipembedzo,keneko kubwalo la Pilato kumene

sadampeze ndi mlandu. Kenaka, adam'tumiza kwa Herodi kumene adamunyoza nam'bwezanso kwa Pilato komwe aYuda adasankha kuti Yesu apachikidwe ndipo Baraba amasulidwe.

Yesu adamusenzetsa mtanda mtanda kupita ku Gologota komwe adamupachika. Yosefe wa ku Arimateya adatenga mtembo wa Yesu nauika m'manda. Atatha masiku atatu, Yesu adauka kwa akufa.

KUFUNIKA KWA IMFA YA YESU

- Idayanjanitsa munthu ndi Mulungu
- Machimo a anthu adakhululukidwa
- Mphamvu ya Mulungu idaonekera
- Pilato ndi Herodi omwe adali pa udani adayanjana
- Imfa idangonjetsedwa

MUTU. 11 CHILENGEDWE

Chilengedwe chimatanthauza zinthu zamoyo ndi zopanda moyo zimene zimapezeka pa malo

ZA CHILENGEDWE ZIMENE ZA ZUNGULIRA SUKULU YANU

1. **ZAMOYO**

   zomera

   anthu

   nyama

2. **Zopanda moyo**

   madzi

   mpweya

   miyala

   mchenga

   kuwala

   dothi

   galimoto

nyumba

MMENE TINGASAMALIRE NYAMA

- pozipatsa chakudya chokwanira
- kuzimangira khola labwino
- kuziteteza ku matenda

Tingasamalire nyama zakuthengo posapha mwachisawawa ,posatentha tchire ndi posadula mitengo kuti tisunge nkhalango.

ZOMWE BAIBULO LIMAPHUNZITSA MMENE TINGASAMALIRE NYAMA

Akhristu amakhulupirira kuti Mulungu adalenga nyama, kuzipatsa chakudya ndikuziika pansi pa ulamuliro wa munthu. Baibulo limaphunzitsa kuti anthu asamachitire nkhaza nyama, chifukwa kumeneko ndikuipa mtima.

END

By emmanuelkapachika

WhatsApp @ 0992077604 for more notes

-